12. Nthambi imapeza mphamvu yake mwa mpesa. Ngati nthambi yadulidwa, imataya mphamvu yake. Tikamadya thupi la Yesu timakhala mwa Iye. Iye ndi mpesa. Ife ndife nthambi zake. Iye amaika mphamvu ya Uzimu mwa ife ndipo timakula mwa mphamvu. Iye amaika mphamvu mwa ife tikamawerenga Buku Lopatulika ndi kumapemphera tsiku ndi tsiku.

Tikamadya thupi lake ndi kumwera mwazi wake, kodi ndi chiyani chimene timatenga kwa Yesu tsiku ndi tsiku?

____________________________________

==========================================================================

13. Ife timatenga mphamvu za uzimu kuchokera kwa Yesu tsiku ndi tsiku. Timachita zimenezi pokhala mwa Iye ndi kumulola kuti Iye akhale mwa ife. Pomawerenga Buku Lopatulika kumatithandiza kuti tikhale mwa Yesu. Kuŵerenga Buku Lopatulika kumafanana monga kudya mkate pamene ife tikhala ndi njala. Nthaŵi zina timachita mantha ndi mavuto a akulu. Kapena mwina timakhala ofooka muuzimu. Ife tikhoza kuwerenga Buku Lopatulika ndipo timalimbikitsidwanso.

Kodi ife timatcha chiyani pamene tikhala mwa Yesu ndi kutenga mphamvu kuchokera kwa Iye tsiku ndi tsiku?

____________________________________

________________________________________________________________

==========================================================================

14. Timakutcha "kudya thupi lake ndi kumwa mwazi wake." Ife timakhala ndi mphamvu tikakhala mwa Yesu ndi Yesu mwa ife. Taonaninso ndime iyi.

Yohane 6:56:

> Iye wakudya thupi langa ndi kumwa mwazi wanga akhala mwa Ine ndi Ine mwa iye.

Kodi chinthu china chachiŵiri chimene ali kutanthauza ndi chotani pamene Iye anati "idyani thupi langa ndi kumwera mwazi wanga?"

(1) Timayenera kulandira Yesu m'miyoyo yathu:

(2) ________________________________________________________

==========================================================================

15. Iye anatanthauzanso kuti ife tizitenga mphamvu kuchokera kwa Iye tsiku ndi tsiku. Timachita zimenezi tikamakhala mwa Yesu ndi kuti Iye akhale mwa ife. Ife sitiyenera kupitiriza kukhala m'machimo ngati tamulandira Yesu m'mitima yathu. Iye adzatipatsa mphamvu kuti tikhale monga momwe amafunira kuti tikhalire.

1 Yohane 2:5-6:

> Koma iye amene akasunga mawu ake, mwa iyeyu zedi chikondi cha Mulungu chathedwa. Mmenemo tizindikira kuti tiri mwa Iye; iye wakunena kuti akhala mwa Iye, ayeneranso mwini wake kuyenda monga anayenda Iyeyu.

Kodi chinthu choyamba ndi chotani chimene Yesu anatanthauza ndi mawu akuti, "Idyani thupi langa ndi kumwera mwazi wanga?"

(1) ______________________________

(2) Tiyenera kutenga mphamvu kuchokera kwa Yesu tsiku ndi tsiku.

==========================================================

16. Chinthu choyamba chimene Yesu anatanthauza chinali chakuti ife tiyenera kumulandira Iye m'miyoyo yathu.

Kodi chinthu chachiŵiri chinali chotani chimene Yesu anatanthauza mwa mawu akuti, "idyani thupi langa ndi kumwera mwazi wanga?

______________________________

==========================================================

17. Chinthu chachiŵiri chimene Iye anali kutanthauza chinali chakuti ife tiyenera kutenga mphamvu kuchokera kwa Yesu tsiku ndi tsiku.

Kodi inu mumatenga mphamvu za uzimu kuchokera kwa Yesu tsiku ndi tsiku?

______________________________

Tsopano tengani nthaŵi ndi kuganizira mosamalitsa bwino za moyo wanu. Lembani zinthu zina zimene zinaonetsa kuti mumatenga mphamvu tsiku ndi tsiku.

______________________________

______________________________

18. Tidzakambirana za yankho lanu mkalasi.

Kodi ndi zinthu ziŵiri ziti zimene Yesu anatanthauza pamene ananena kuti "idyani thupi langa ndi kumwera mwazi wanga?

(1) ________________________________________

(2) ________________________________________

SABATA LA KHUMI: KHRISTU, MKATE WA MOYO
TSIKU LACHINAYI: PAMENE AMBIRI ANABWERERA M'MBUYO KHUMI NDI AŴIRI ANATSALA

1. Dzulo tinaphunzira za kulankhula kwa Yesu pa za mkate wa moyo. Ife tinaphunzira zomwe Yesu anatanthauza pamene Iye anati, "Idyani thupi langa ndi kumwera mwazi wanga."

Kodi Iye anatanthauza chiyani?

(1) ____________________

(2) ____________________

==========================================================================

2. Yesu anatanthauza kuti ife tiyenera kulandira Yesu m'miyoyo yathu. Iye anatanthauzanso kuti ife tiyenera kutenga mphamvu kuchokera kwa Yesu tsiku ndi tsiku.

Lero tiona kuti anthu a mitundu iŵiri anamvera Yesu. Anthu ena anabwerera m'mbuyo pamene anamva Yesu ali kulankhula. Koma khumi ndi aŵiriwo anakhala naye. Lero tiphunzira zifukwa ziŵiri zimene akuphunzira anakhalira ndi Yesu.

(1) Yesu ali ndi mawu amoyo wosatha.
(2) Yesu ndi woyerayo wa Mulungu.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Yohane 6:60 kulekeza 69. Ŵerenganinso ndime 60.

Kodi otsatira Yesu ambiri ananena chiyani pamene iwo anamva mawu a Yesu?

____________________

==========================================================================

3. Ambiri a iwo anati, "chinthu chimenechi ndi chovuta." Iwo anamva mawu a Yesu akuti, "idyani thupi langa ndipo imwani mwazi wanga." Iwo sanamvetsetse chimene Iye anali kutanthauza.

Yohane 6:52:
Pamenepo Ayuda anatetana wina ndi mnzake ndi kunena "Akhoza bwanji ameneyu kutipatsa ife kudya thupi lake?"

Yohane 6:66:

Pa ichi ambiri akuphunzira ake anabwerera m'mbuyo, ndipo sanayendayendanso ndi Iye.

Kodi ophunzira ambiri anachita chiyani pamene anamva mawu a Yesu za mkate wa moyo?

________________________________________________

====================================================================

4. Ambiri a iwo anabwerera m'mbuyo. Iwo sanatsatirenso Yesu.

Chimenechi ndi chomwe Musa anachita. Musa anapita ku sukulu ya Buku Lopatulika ku Nigeria. Iye anafuna kukaphunzira zina za Mulungu. Poyamba iye anaphunzira ntchito zabwino zomwe Yesu anachita pa dziko lapansi. Iye anali wokondwa pakumva za chimenechi. Iye anafuna kuti Yesu amuchitire zinthu zabwinonso. Ndipo Musa anamva kuti Yesu anafera zochimwa za anthu. Iye anauzidwa kuti atenge Yesu monga nsembe ya machimo ake. Musa sanathe kulandira chiphunzitso chimenechi. Iye anaganiza kusiya sukulu.

M'Buku Lopatulika, kodi ndi ndani anatembenuka kusiya kutsatira Yesu pamene iwo anamva mawu ake olimba?

________________________________

====================================================================

5. Ena mwa otsatira a Yesu anatembenuka ndi kumusiya. Analipo ambiri amene anachita zimenezi. Iwo anati mawu a Yesu anali ovuta kuŵamvetsetsa. Koma khumi ndi aŵiriwo anakhala ndi Yesu.

Yohane 6:67-68:

Yesu anati kwa khumi ndi aŵiriwo, "Nanga inunso mufuna kuchoka?" Simoni Petro anamyankha Iye, "Ambuye, tidzamuka kwa yani? Inu muli nawo mawu a moyo?

M'ndime imeneyi, kodi Petro anati Yesu ndi ndani?

____________________

====================================================================

6. Iye anati Yesu ali ndi mawu a moyo wosatha. Anthu ambiri amene anatsatira Yesu anabwerera m'mbuyo. Iwo sanafune kumutsatiranso. Koma panali ena amene anali kuyamba kumvetsetsa. Iwo anakumbukira zomwe Yesu

ananena.

Yohane 6:63:
Mawu amene ndalankhula ndi inu ndiwo Mzimu ndi moyo.

Kodi ndani anakhala ndi Yesu chifukwa iye ali ndi mawu a moyo wosatha?

______________________________________________________________
==============================================================

7. Akuphunzira khumi ndi aŵiri ndiwo anachita zimenezi. Chimenechi ndi chikumbutso cha asungwana aŵiri, Sara ndi Naomi. Iwo anali ophunzira a sukulu ya sekondare ya ku Nigeria. Iwo ndiwo anali Akhristu pakati pa ophunzira onse. Koma ena mwa aphunzitsi anali Akhristu. Chaka chimodzi kunalibe mvula. Mkulu wapa sukulupo anafunsa anyamata a sukulu kuti ikatha sukulu ayambe atsalira kuti apempherere mvula. Pa tsiku loyamba ophunzira ambiri anatsalira, koma pasanapite nthaŵi iwo anapita kwawo. Anali Naomi ndi Sara yekha amene anatsalira pamodzi ndi mphunzitsiyo. Iwo anati ndi Yesu yekha amene akadapereka mvula. Sara ndi Naomi anatsalira monga ophunzira khumi ndi aŵiri anachitira. Iwo asanathe kupemphera, mvula inayamba.

Kodi ophunzira khumi ndi aŵiri anakhala ndi yani amene ali ndi mawu amoyo wosatha?

______________________________________________________________
==============================================================

8. Iwo anakhala ndi Yesu. Iwo anali kuyamba kumvetsetsa kuti Yesu anali ndani. Nazi zimene iwo ananena.

Yohane 6:68-69:
Inu muli nawo mawu amoyo wosatha. Ndipo ife tikhulupirira ndipo tidziŵa kuti Inu ndinu Woyera wa Mulungu."

Ophunzira khumi ndi aŵiri anakhala ndi Yesu, kodi Iye ali ndi mawu otani?

______________________________________________________________
==============================================================

9. Yesu ali ndi mawu amoyo wosatha. Iye ndi yekhayo amene angawapatse anthu moyo wa mtundu umenewu. Palibe njira inanso yopitira kumwamba koma kupyolera mwa Yesu.

Yohane 14:6:

> Yesu ananena naye ... "Ine ndine njira ndi choonadi ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate koma mwa Ine."

Lembani chifukwa choyamba chimene ophunzira khumi ndi aŵiri anakhalira ndi Yesu. Ndipo werengani chachiŵiricho.

(1) ______________________________

(2) Yesu ndi Woyerayo wa Mulungu.

==========================================================================

10. Ophunzira khumi ndi aŵiri anakhalira chifukwa Yesu ali ndi mawu amoyo. Iwo anakhulupirira mawu ameneŵa. Iwo anayamba kumvetsetsanso kuti Yesu ndi ndani. Petro anati Yesu ndi Woyera wa Mulungu. Iye pone-na zimenezi ananenera ophunzirawo. Iwo anayamba kumvetsetsa kuti Yesu ndi Mulungu.

Kodi ophunzira ena anayamba kuchita chiyani, amene sanakhulupirire kuti Yesu ndi Woyerayo wa Mulungu?

______________________________

==========================================================================

11. Iwo anabwerera m'mbuyo. Iwo sanadziwe kuti Yesu ndi ndani. Koma ophunzira khumi ndi aŵiriwo anatsalira. Iwo anatsatirabe Yesu. Tiyeni tionenso zomwe Petro ananena pamene iye analankhula m'malo mwa khumi ndi aŵiriwo.

Yohane 6:68.69:

> Inu muli nawo mawu amoyo wosatha. Ndipo ife tikhulupirira, ndipo tidziŵa kuti Ine ndinu Woyera wa Mulungu.

Kodi Petro ananena kuti Yesu ndani? ______________________________

==========================================================================

12. Petro anati Yesu ndi Woyera wa Mulungu. Kunena kuti Woyera wa Mulungu kumatanthauza kuti Iye ndi Mulungu. Ophunzira anaona mphamvu yaikulu ya Yesu. Iwo anaona chikondi chake pa anthu. Ndi Mulungu yekha akanakhoza kuchita zinthu zimene anaziona Yesu akuchita.

Chifukwa chakuti iwo anamvetsetsa chimenechi, kodi ophunzira khumi ndi aŵiriwo anachita chiyani pamene ena anatembenuka ndi kumusiya Yesu?

______________________________________________

==============================================================

13. Iwo anakhala ndi Yesu. Mwina nthaŵi imeneyi inali yovuta kwa iwo. Koma iwo anakumbukira zomwe iwo anaziona ndi kuzimva. Ndi Mulungu yekha akanakhoza kuchita zozizwa zimene anaziona.

Kodi ndani amene ali Woyera wa Mulungu?

______________________________

==============================================================

14. Woyera wa Mulungu ndi Yesu. Chimenechi ndi chifukwa chachiŵiri chomwe ophunzira anakhalira ndi Yesu. Yesu anatumizidwa ku dziko lapansi kudzaphunzitsa anthu za mkate wamoyo. Woyera wa Mulungu anatumizidwa kuti anthu ake akhoza kudya thupi lake ndi kumwera mwazi wake." Petro anali kunena kuti Yesu anakwaniritsa malonjezo onse amene anakonzedwera a Israeli.

Kodi ndani amene anatumiza Woyerayo?______________________________

==============================================================

15. Amene anamutumiza ndi Mulungu.

Yohane 6:57-58:

> Monga Atate wamoyo ananditumuma Ine, ndipo Inenso ndiri ndi moyo chifukwa cha Atate; momwemo wondidya Ine, iyeyu adzakhala ndi moyo chifukwa cha Ine. Mkate Wotsika kumwamba ndi umenewu si monga makolowo, anadya namwalira; iye wakudya mkate umene adzakhala ndi moyo nthaŵi zonse.

Pamene Yesu analankhula za mkate wamoyo, ophunzira ena anamusiya Iye. Kodi chifukwa china chachiŵiri chomwe ophunzira anakhalira naye ndi chiyani?

(1) Yesu anali mawu amoyo wosatha

(2) ____________________

================================================================

16. Chifukwa chachiŵiri ndi chakuti Yesu ndi Woyerayo wa Mulungu. Ophunzira anaona chimenechi. Iwo anayamba kumvetsetsa. Iwo anati kwa Yesu, "Inu ndinu Woyera wa Mulungu.

Kodi ndi chifukwa chiti choyamba chomwe ophunzira khumi ndi aŵiri ananena kuti iwo ayenera kukhala ndi Yesu? ____________________

____________________

================================================================

17. Chifukwa choyamba ndi chakuti Yesu ali ndi mawu amoyo wosatha. Iye ndiye yekhayo amene angapatse moyo anthu. Pali njira imodzi imene tingapatse moyo anthu. Pali njira imodzi imene tingapitire kumwamba.

Kodi chifukwa chachiŵiri ndi chotani chimene ophunzira khumi ndi aŵiri anati akhalira ndi Yesu?

(1) Yesu ali ndi mawu amoyo.

(2) ____________________

================================================================

18. Chifukwa chachiŵiri ndi chakuti Yesu ndi Woyera wa Mulungu. Mphunziro ili tikuona kuti ophunzira anali kukula. Iwo anayamba kuona kuti Yesu ndani. Iwo anaona chikondi chake cha pa anthu. Iwo anaona mphamvu yake yaikulu. Kodi bwanji ife? Tiyenera kudzifunsa ngati tinaona chikondi cha Yesu ndi mphamvu yake. Tiyenera kuganiza za mmene Yesu alili. Ife tiyenera kukhala ndi Yesu kuti tione zimenezi.

Tsopano yambani mwaima ndi kuganizira za moyo wanu. Kodi inu muli kukhala ndi Yesu?

_________________________________________________

Kodi inu mumakhala wokhulupirika pomapita ku misonkhano yonse ku tchalitchi kwanu kukapembedza Mulungu ndi kukaphunzira mawu ake?

______________________________

==========================================================================

19. Pa Yohane 6, pamene Yesu analankhula za mkate wamoyo, akuphunzira ena anamsiya Iye. Kodi ndi chifukwa chiyani ophunzira khumi ndi aŵiri anati iwo akhala naye?

(1) __________________________________________________________

(2) __________________________________________________________

==========================================================================

SABATA LA KHUMI: KHRISTU, MKATE WA MOYO
TSIKU LACHISANU: KUBWEREZA

1. Tsopano mwatsiriza theka la moyo umene Khristu anakhala nawo m'dziko lapansi. Pali zinthu zina zambiri zoyenera kuphunzira, koma mwaphunzira kale zambiri. Mwachita bwino kwambiri kudzafika pamenepa. Yesu ndiye munthu wamkulu woposa aliyense amene anakhala. Iye anali Mulungu ndipo Iye ndi Mulungu. Lolani kuti chiphunzitso chamoyo wake chilowe pansi pa moyo wanu. Mukondeni ndi kumumvera Iye nthaŵi iliyonse.

Tsopano ndi nthaŵi yobwereza maphunziro a bukuli. Tiyamba ndi sabata Lachisanu ndi Chinayi ndi Sabata la Khumi. Ndipo tibwerezenso mbali ina yotsala ya bukuli. Mutenge masiku omwe mungabwerezere bukuli.

Lembani yankho la funso lililonse. Ndipo mubwerere kuphunziro kuona ngati mwalondola.

MAFUNSO OCHOKERA PA SABATA LACHISANU NDI CHINAYI:

1. Kuchokera ku chiphunzitso cha Yesu kwa Simoni Mfarisi ndi mkazi wochimwa, kodi ife tiyenera kukhala ndi chiyani kuti tikhululukidwe?

   ________________________________________

   Kodi kukhala wokhululukidwa kumaika chiyani mumtima mwa wokhulupirirayo?

   ________________________________________

2. Kuchokera ku nthano ya namsongole, kodi chidzaoneka ndi chiyani kwa namsongole kapena ana a woipayo pachimaliziro chawo?

   ________________________________________

   Kodi ndi chiyani chidzaoneke kwa mbewu yabwino kapena kwa ana olungama a Mulungu?

   ________________________________________

3. Kodi ndi phunziro lotani limene Yesu anaphunzitsa ponena nthano ya chuma chobisika ndi ngale ya mtengo wapatali? ________________

   ________________________________________

4. Zozizwitsa zinayizi zinalembedwa pa Luka 8. Kutontholetsa mphepo, kumasula munthu wotchedwa Legio, kuchiza mkazi wa nthenda, kuutsa mwana wa mkazi wa Yairo. Kodi zomwe zimaonetsa mphamvu ya Yesu zimaonetsa kuti anaposa chiyani?

(1) ____________ (3) ____________

(2) ____________ (4) ____________

5. Pa Luka 9:2, kodi Yesu anatuma ophunzira khumi ndi aŵiri kuti atuluke kukachita chiyani?

(1) ____________

(2) ____________

MAFUNSO A SABATA LA KHUMI:

6. Kodi ndi zinthu ziŵiri zotani zomwe zozizwa za kudyetsa unyinji wa anthu zikwi zisanu umatiphunzitsa za Yesu?

(1) ____________

(2) ____________

7. Kuchokera pa chozizwa chakuti Yesu anayenda pamadzi ndi kuti anatontholetsa mphepo, kodi timaphunzira chiyani za mavuto?

(1) ____________

(2) ____________

8. Kodi Yesu anatanthauza zinthu ziŵiri zotani pamene Iye anati "Idyani thupi langa ndipo imwani mwazi wanga?

(1) ____________

(2) ____________

9. Pamene Yesu analankhula za mkate wamoyo, ophunzira ena anamuchokera Iye namusiya. Kodi ndi chifukwa chiyani ophunzira khumi ndi aŵiri anakhala ndi Yesu?

(1) ____________

(2) ____________

Pamene mwadziŵa mayankho onseŵa, bwereraninso ku tsamba 93,191,260, ndi 261. Bisani mayankho amene mwalemba. Yesani kulemba mafunso onse. Ngati mungathe kuyankha onsewo ndiye kuti mwaphunzira bwino.